



Khadi Lapafupi Lachiwerengero Chida Chothandizira Malawi

Mark Schreiner

1 Julai 2019

Chikalata ichi na chakutebetesya kupokelelapo mauhtenga chanozyeka mu chiyoboyero cha muchitumbuka pa scorocs.com

This document and a data-collection tool are in English at scorocs.com

Chikalata ichi ndi mfundo zakafukufuku zosonkhanitsidwa zipezeka mu Chichewa pa kangaude wa scorocs.com

Scorocs ndiwo ena ake a Khadi Lapafupi Lachiwerengero chida chothandiza kuona pa za umphawi (*the Scorocs Simple Poverty Scorecard®-brand poverty-assessment tool*) makamaka mokhudzana ndi ndondomeko zothandiza osauka m'dziko la Malawi pofuna kuthandiza ndi kutukula umoyo wawo pakugwapo potengako mbali pa zochitika. Mayankho okhudzana ndi mafunso 10 amu khadi ili akhoza kusonkhanitsidwa pa mphindi 10 chabe ndi kugwiritsidwa ntchito pakuona ndi kuyerekeza manambala ya milingo pa umphawi wodza chifukwa chakusowekera kwa chakudya, ndi kuona zisintho zimene zachitika zokhudzana ndi umphawi, kapena kuona pa zosinthika za wotengako mbali payekhapayekha.

Chiganizo chimenechi

Khadi ili la chiwerengero ndi latsopano la dziko la Malawi lakonzedwa ndi mfundo zakafukufuku zosonkhanitsidwa m'chaka cha 2016/17. Iyenera kugwiritsidwa ntchito kuchokera tsopano lino, kutenga malo a khadi lachiwerengero chakale cha Schreiner (2015a) chimene chinasonkhanitsidwa ndi mfundo zakafukufuku za m'chaka cha 2010/11. Ogwiritsa ntchito asayerekezere zisintho za ziwerengero zaumphawi kwa nthawi yaitaliko pogwiritsa ntchito zosonkhanitsidwa zakale za 2010/11 za khadi la chiwerengero (kapena za khadi lakale lachiwerengero cha 2004/5) koma atsatire zotsopano za khadi la chiwerengero latsopano la 2016/17.

Mayamiko

Pepala ili lidakonzedwa ndi thandizo la ndalama zochokera ku bungwe la Private Sector Window of the Global Agriculture and Food-Security Program, ndi bungwe lina la International Finance Corporation. Mfundo za kafukufuku zinasonkhanitsidwa ndi bungwe la Malawi National Statistical Office ndipo zinatsitsidwa pa webusaiti ya World Bank Central Microdata Catalog. Chiyamiko chipite kwa Yanni Chen, Habtamu Fuje, Talip Kilic, and Heather Moylan. [Japhet Mphande](#) wamasulira zonsezi kuzipereka mu Chichewa.

Scorocs® Khadi Lapafupi Lachiwerengero Chida Chothandizira

Interview ID: _____	Name _____	Identifier _____
Interview date: _____	Participant: _____	_____
Country: MWI	Field agent: _____	_____
Scorecard: 003	Service point: _____	_____
Sampling wgt.: _____	Nambala ya mamembala apanyumba: _____	

Choonetsera	Yankho	Mapointsi
1. Kodi banja lonse lapanyumba mukukhala mu tauni iti?	A. Chitipa, kapena Karonga	0
	B. Neno, Nkhata Bay, Nsanje, Phalombe, kapena Rumphu	4
	C. Chiradzulu, Machinga, kapena Thyolo	6
	D. Balaka, kapena Mangochi	8
	E. Chikwawa, kapena Dedza	9
	F. Nkhotakota, kapena Salima	11
	G. Mzimba, Ntcheu, kapena Ntchisi	12
	H. Dowa, Kasungu, Mchinji, Mwanza, Zomba, kapena Zomba City	13
	I. Blantyre, Lilongwe City, kapena Mulanje	15
	J. Blantyre City, Lilongwe, kapena Mzuzu City	17
2. Kodi panyumba pano pali mamembala angati?	A. Seveni kapena opitilirapo	0
	B. Sikisi	5
	C. Asanu	9
	D. Anayi	15
	E. Atatu	20
	F. Awiri	27
	G. M'modzi	41
3. Kodi yanthawi ya nyengo yakutentha ikafika monga mu Oktoba, mukulu wolamulira pa nyumba amagona poti?	A. Nsalu ya chitenje, saka ya thumba la fataleza kapena la mbeu, zovala, palibe, kapena zina	0
	B. Gombeza chabe	2
	C. Gombeza ndi nsalu zapabedi, kapena nsalu zapabedi chabe	5
4. Mu miyezi khumi ndi iwiri yapitayi, kodi mwamuna wolamulira pa nyumba (kapena mwamuna wa mkazi wolamulira) anagwirako zintchito za kanthawi, kapena ganyu, ngakhale kwa ola limodzi chabe?	A. Inde	0
	B. Palibe mwamuna wolamulira (ndipo mkazi wolamulira panyumbapo alibe mwamuna)	0
	C. Ai	4
5. Kodi mkazi wamkulu wolamulira (kapena mkazi wamkulu wa mwamuna wolamulira) akwaniritsa kuwerenga ndi kulemba Chichewa kapena Chingerezi?	A. Ai	0
	B. Chichewa chabe	2
	C. Palibe mkazi wolamulira (ndipo bambo wolamulira panyumbapo alibe mkazi)	2
	D. Chingerezi chabe, kapena zonse Chingerezi ndi Chichewa	4
6. Kodi nyumba yokhalamo ili ndi denga lopangidwa ndi chiani? (<i>onani ndipo lembani</i>)	A. Udzu	0
	B. Malata, matayilosi adothi, konkili, mapulasitiki, kapena zina	3
7. Kodi muli ndi gome pa nyumbayi?	A. Ai	0
	B. Inde	2
8. Kodi panyumbapo pali makama angati?	A. Palibe	0
	B. M'modzi	5
	C. Awiri kapena opitilirapo	10
9. Kodi muli ndi mipeni za malupanga (zikwanje/mapanga) pa nyumba pano?	A. Ai	0
	B. Inde	3
10. Kodi panyumbapo pali maselefoni angati omwe akugwira ntchito pa nyumba?	A. Palibe	0
	B. Imodzi	6
	C. Awiri kapena opitilirapo	11

Pepala Lakumbuyo Logwiritsa Ntchito: Mamembala a Panyumba

Filani pamwamba pa khadi lachiwerengero choyamba. Muonjezepo chizindikiro chakufunsana (ngati ncodziwika), tsiku lofunsa, komanso nambala la chiwerengero chonse cha anthu apanyumba moimirako panyumba pomwe mwafunsa wotengako mbali (ngati nzodziwika). Mukatero, mulembe dzina lonse ndi nambala lake lapadera la wotengako mbali (amene mwina satha kukhala oyankha), wa gawo la ajenti wotengako mbali (amene akhoza kusiyana ndi wowerengetsera), ndi sevisi pointi yomwe wotengako mbali akugwiritsa ntchito (ngati ndiyodziwika). Mulembe muzongulira yankho pa choonetsera cha pa khadi lachiwerengero molingana ndi tauni komwe banja likukhala.

Tsopano muwerenge kwa oyankha: *Chonde ndiuzeni maina anu oyamba (kapena maina opeka) a onse mamembala apanyumba, kuyambira pa wolamulira ndi amwao aakulu paonse (ngati alipo m'modzi). Nyumba ndi munthu m'modzi, kapena gulu la anthu (zilibe kanthu ndi abanja limodzi kapena ai, ndi wokwatirana kapena ai) omwe amakhala ndi kudyera limodzi zao.*

Lembani dzina loyamba/dzina lopeka la membala aliyense, kuyambira ndi wolamulira (wamkulu) wamwao wa wolamulira (ngati alipo). Chongani wolamulira wamwamuna (kapena mwamuna wa wolamulira wamkazi, ngati aliko), ndipo muchongenso mkazi wolamulira (kapena mkazi wamkulu wa mwamuna wolamulira, ngati aliko). Lembani nambala ya apanyumba mu mutu wa khadi lachiwerengero pafupi ndi "Nambala ya mamembala apanyumba:". Mukatero mulembe mozungulira yankho pa choonetsera chachiwiri pa khadi lachiwerengero za nambala ya mamembala apanyumba.

Muwerenge mokweza mawu funso lachitatu, lachinayi, ndi lachisanu, ndipo mulembe mayankho ya oyankha. Mulembe yankho la funso la nambala sikisi lokhudzana ndi zomwe adapangira denga, mufunse oyankha pokhapo simuli kuona ndi kuzindikira bwino mutayangana. Potsiriza, werengani mokweza mawu mafunso anambala seveni, eiti, naini, kufikira la khumi, ndi kulemba mayankho ya oyankha.

Nthawi zonse kumbukirani ndi kulondola mozama malamulo opatsidwa mu "Zotsogolera Pofunsa".

Dzina loyamba kapena dzina lopeka	Mkulu wolamulira kapena a amwao mwa mkulu wolamulira
1.	Mkulu wolamulira (mwamuna) Mkulu wolamulira (mkazi)
2.	Mkazi wamkulu wa mwamuna wolamulira Mwamuna wa wamkazi wolamulira Zina
3.	Zina
4.	Zina
5.	Zina
6.	Zina
7.	Zina
8.	Zina
9.	Zina
10.	Zina
11.	Zina
12.	Zina
13.	Zina
14.	Zina
15.	Zina
16.	Zina
Nambala ya mamembala apanyumba:	—

Zotsogolera Pofunsa

Nusu zonedwa kale munsimu zacokera:

National Statistical Office. (2016) "Enumerator Manual for the Household Questionnaire: Fourth Integrated Household Survey, 2016/17", microdata.worldbank.org/index.php/catalog/2936/related_materials, retrieved 5 May 2019 [la *Buku Lomasulira*].

Malangizo wofunikira pofunsa

Khadi lachiwerengero likhoza kulembedwa mkati pomwe mukugwira ntchito imeneyi, ndi mayankho kulowetsedwa pambuyo pake mu spreadsheet kapena mudatabesi yanu. Komanso, pali kachida ka Scorocs kosungiramo mfundo zakafukufuku koma kamagwiritsidwa ntchito mu webu kapena pa mafoni aja odziwika kuti Android, omwe mukhoza kulowetsamo mfundo zakafukufuku pomwe mukugwira ntchito kapena pomwe muli mu ofesi. Ngati palibe mphamvu zolumikizitsa, mfundo zakafukufuku zizasungidwa kufikira mutapeza mphamvu zolumikizitsira pa intaneti. Yesani chida chotenga mfundo za kafukufuku, kapena funsani za akaunti ya pulayiveti.

Monga mwa tsamba 5 la *Buku Lomasulira*, [khadi lachiwerengero] iyenera kulembedwa mukati pamene muli pompo pa nyumba ya oyankha.

Khadi lachiwerengero liyenera kugwiritsidwa ntchito ndi wochititsa chiwerengero yemwe ndi wophunzitsidwa kulondola "Zotsogolera Pofunsa".

Lembani pamwamba pa khadi lachiwerengero ndi pa "Pepala Lakumbuyo Logwiritsa Ntchito" choyamba, potsatira malangizo opezeka pa "Pepala Lakumbuyo Logwiritsa Ntchito".

Mu mutu wa khadi lachiwerengero, lembani nambala ya mamembala apanyumba potsatira mndandanda omwe munakonza pa "Pepala Lakumbuyo Logwiritsa Ntchito".

Musafunse molunjika funso loyamba la pakhadi lachiwerengero (“Kodi banja lonse lapanyumba mukukhala mu tauni iti?”). Koma lembani yankho mogwirizana ndi maganizo anu pa malo kumene nyumbayo ili.

Chimodzimidzinsu, musafunse molunjika funso lachiwiri la pakhadi lachiwerengero (“Kodi panyumba pano pali mamembala angati?”). Koma lembani yankho mogwirizana ndi nambala ya mamembala omwe munalembe pa mndandanda pa “Pepala Lakumbuyo Logwiritsa Ntchito”.

Mafunso onse wokhalira mufunse oyankhayo molunjika, kuchotsako funso la sikisi (“Kodi nyumba yokhalamo ili ndi denga lopangidwa ndi chiani? (*onani ndipo lembani*)”). Funsoli, yesetsani kuona pa nokha poona mmene denga lili. Ngati yankho siili kuoneka bwino, chonde funsani oyankhayo.

Monga mwa tsamba 24 la *Buku Lomasulira*, “Werengani mafunso mofanana ndi momwe alembedwera mu [khadi lachiwerengero], potsatiranso ndondomeko yake.”

Zoikika zotsogolera pofunsa

Santhulani “Zotsogolera Pofunsa” izi mosamala, ndipo muyenera kunyamula pomwe mukugwira ntchito. Londolani malangizo amkati mwa “Zotsogolera Pofunsa” (kuonjezapo langizoli).

Chili bwino kwa oyankha kukhala wotengako mbali mu bungwe, komanso ndi chabwinonso kuti oyankha akhala membala wina wa panyumba amene si ali membala wa panyumba amene si ali wotengako mbali mu bungwe.

Chimodzimidzi, ajenti woyendera amene ayenera kulembedwa mu mutu wa khadi lachiwerengero sikuti ameneyu mpaka akhalebe wosafanana ndi wowerengetsera amene achititsa kufunsaku. Koma ajenti woyendera uyu ndi nyantchito wa pologalamu ya aumphawi imene wotengako mbali ali nalo paubale. Ngati palibe ajenti woyendera, ndiko kuti musalembemo mumalowo mu mutu wa khadi lachiwerengero, malowo akhale opanda kanthu.

Werengani funso lililonse mwatsatanetsatane, monga momwe zalembedwera mu khadi lachiwerengero.

Mukalemba yankho pa khadi lachiwerengero, lembani nambala ya pointi mum'ndandanda wa "Score" ndipo mulembe mozungulira yankho, nambala yosasindikizidwa, ndi mapoints yomwe mwalemba, motere:

8. Kodi panyumbapo pali makama angati?	A. Palibe	0	
	B. M'modzi	5	5
	C. Awiri kapena opitilirapo	10	

Kuchepetsako zolakwika, muyenera:

- Kulemba mapoints yomwe yagwirizana ndi mayankho mu mndandanda wakudzanja lamanja
- Kulemba mozungulira mayankho yomwe siyanasindikizidwe, ma points yomwe siyanasindikizidwe, komanso mapoints wolembedwa ndi inu

Pakabwera nkhani yomwe siinafotokozedwe mu "Zotsogolera Pofunsa", wowerengetsera apange chiganizo, pakuti zimenezo ndizo zimene zimachitika mu Malawi NSO mu 2016/17 IHS. Ndiko kuti bungwe logwiritsa ntchito khadi lachiwerengero lisapange malamulo ena (osiyana ndi awa opezeka mu "Zotsogolera Pofunsa") omwe ndiwo adzagwiritsidwa ntchito ndi onse ochititsa chiwerengero. China chilichonse chosafotokozedwa mu Zotsogolera Pofunsa, zikhalira kwa wowerengetsera kupanga chiganizo.

Musawerenge mayankho kwa oyankha. Koma werengani funso, ndipo muyime kaye; dikirani yankho. Ngati oyankha akupempha kuti amvetsetse kapena akulumaluma kapena akuoneka kusokonekera, ndiye werengananinso funso kapena thandizirani monga mwa Zotsogolera Pofunsa kapena monga inu, pokhala wowerengetsera, mukuonera kuyenera.

Monga mwa zonse, landirani mayankho opatsidwa ndi oyankha. Koma ngati oyankha akunena zina – kapena mukaona kaya kuzindikira china chake – choonetsa kuti yankho mwina yaphonyeka, kapena kuti oyankha akukaika, kapena kuti oyankha akufuna thandizo mmene angayankhire, pamenepo muwerengenso funso ndipo mupereke thandizo limene mungaone kuti ndilo loyenera monga mwa “Zotsogolera Pofunsa”.

Mwina mayankho ambiri pa mafunso amu khadi lachiwerengero ndi otsimikizidwa, pa nthawi zambiri simuyenera kutsimikizira mayankho. Muyenera kutsimikizira pokhapo paoneka kanthu koonetsa kuti mwina yankho laphonyeka ndipo mudzatero kuti kutsimikizirako kuthandizire kulungamitsa mfundo zosonkhanitsidwazi. Mwa chitsanzo, mungathe kusankha kutsimikizira ngati oyankha akunena molumaluma, akuonetsa mantha, kapenanso akuonetsa kuti akunama, wasokonekera, kapena akukaika. Momwemo chitsimikizo ndichofunika ngati mwana panyumbapo kapena ngati mnansi wanena mawu ena omwe sanagwirizane ndi mawu a oyankha. Kutsimikizira ndi chinthu chabwino ndithu ngati inuyo mwaona kanthu koonetsa kuti yankho mwina yaphonyeka, monga katundu wina omwe munthuyo ali nawo, kapena mwana amene alinkudya mchipinda koma sanawerengeredwe ngati membala wa panyumbapo.

Monga mwa zonse, kufitsa kwa khadi lachiwerengero kuyenera kulondola pafupi kwambiri ndi kufitsa kwa 2016/17 IHS ya Malawi NSO. Mwa chitsanzo, mafunso aperekedwe ndi munthu wophunzitsidwa ukadaulo wachiwerengero panyumba ya wotengako mbali chifukwa zimenezo ndizo zimene a NSO anachita mu 2016/17 IHS.

Kumasulira

Pa nthawi ya kulemba khadi lachiwerengero ili, “Pepala Lakumbuyo Logwiritsa Ntchito”, ndi “Zotsogolera Pofunsa” izizi zikupezeka mu Chingerezi, Chichewa, ndi Chitumbuka. Sizinakhale m’ malo mwake pakali pano, aukadaulo wakumasulira zilankhulo zina zolankhulidwa m’ dziko la Malawi monga Chinyanja ndi Chiyao. Ogwiritsa ntchito aone pa scorocs.com kuona kuti ndi ziti zina zimene zamasuliridwa kuchokera pomwe izizi zinalembedwa.

Ngati palibe zina zovomereza, aukadaulo wa zomasulira m’ chilankhulo chofunika, pomwepo ogwiritsa ntchito alumikizane ndi Scorocs kuthandiza kupanga kumasulira kumeneko.

Monga mwa tsamba 16 la *Buku Lomasulira*, “[Khadi lachiwerengero] linakonzedwa mu Chingerezi, [Chichewa, ndi Chitumbuka]. Manyumba ambiri komwe mudzapita kukasonkhanitsa zofunikira za [khadi lachiwerengero] sadzatha kuyankha mu Chingerezi ngati mudzafunsa mafunso mu Chingerezi. Chomwecho, muyenera kumasulira mafunso m’chilankhulo chimene mamembala apanyumbapo akudziwa kwambiri. Pali mfundo zitatu zoyenera kusunga.

“Choyamba, pali mawu angapo ofunikira kwambiri kudziwa amenenso aonekera ponseponse mu [khadi lachiwerengero]. Pamawuwo pali *panyumba, mkulu wolamulira panyumba, [umphawi, ndi umoyo]*.

“Mawuwa nthawi zonse ayenera kumasuliridwa mu chilankhulo cha kumalo kumeneko pogwiritsa ntchito mawuwo mosasintha konse. Mafunso mu Chingerezi akonzedwa mosamalitsa kwambiri pofunitsitsa kuona kuti zotulukamo zikulondola cholinga chake cha ganizo ili. Santhulani mafunso potero kuti mufunse bwino kopanda kusintha kena kalikonse. Ngati sizitero, ndiko kuti mayankho apanyumba zosiyana-siyana siyangathe kufananitsidwa.

[Pa tsamba 107–108 la *Buku Lomasulira*, a NSO akonza mmene mawu ena ayenera kumasuliridwa mu Chichewa, Chitumbuka, ndi mu Chiyao:]

English	Chichewa	Chitumbuka	Chiyao
Head of household	Mkulu wolamulira mnyumba kapena pa banja	Uyo wali namazaza	Mtwee waliwasa; jwakulamulila pewasa
Household	Panyumba; banja	Banja	Nyumba/liwasa
Respondent	Oyankha	Wakuzgora	Wakwanga iusyo
Poverty	Umphawi	Ukavu	Kulaga; usauchi; yakunonopa
Welfare	Cikhalidwe; umoyo	Ukhaliro	Chisamalilo

“Chachiwiri, [khadi lachiwerengero] liyenera kufotokozeredwa mu chilankhulo chimene mamembala ofunsiidwa apanyumbapo akudziwa kwambiri. . . . Dziwitsani wokutsogolerani ngati simutha kulankhula bwino chilankhulo chimene apanyumbapo akudziwa kwambiri.

“Potsiriza, musayeserere kuti kudziwa Chichewa kwanu kudzalola kuti mufunse mafunso m’dziko lonse la Malawi. Ngakhale kuti Chichewa ndi chilankhulo cha dziko la Malawi, anthu ambiri m’malo akumidzi satha kulankhula bwino kwambiri chilankhulochi. Zimenezi ndizoonadi makamaka kumpoto kwa Malawi (kumene Chichewa sichilankhulidwa mofala) komanso m’mbali mwa Nyanja (kumene Chiyao chimalankhulidwa kwambiri m’midzi). Dziwitsani wokutsogolerani ngati simutha kulankhula bwino chilankhulo chimene apanyumbapo akudziwa kwambiri.”

Kodi oyankha ayenera kukhala yani?

Chili bwino kwa oyankha kukhala wotengako mbali mu bungwe, komanso ndi chabwinonso kuti oyankha akhala membala wina wa panyumba amene si ali membala wa panyumba amene si ali wotengako mbali mu bungwe.

Monga mwa tsamba 32 la *Buku Lomasulira*, amene ayenera kuyankha bwino funso lofunsidwa ndi “munthu wa panyumbapo amene akudziwa bwino mutu wa nkhaniyo.”

Mafunso a mukhadi lachiwerengero, la *Buku Lomasulira* lionetseratu poyera kuti, pa zonse komanso ngati palibe mfundo zounikirira, mkulu wolamulira mnyumba kapena banja ndiye membala wodziwa bwino kwambiri panyumbapo motero yemweyo ndiye ayenera kuyankha. Ngati mkulu wolamulira mnyumba palibe, pamenepo *Buku Lomasulira* likuti “ngati pali amwao a mkulu wolamulira mnyumba kapena banja, ndiko kuti amenewo ndiwo ayenera kawmbiri kukhala oyankha” kapena kuti wina amene atha kuyankha ndiye “munthu wamkulu pakati pa mamembala onse mnyumbamo amene ali pompo”.

Monga mwa tsamba 55 la *Buku Lomasulira*, mkulu wolamulira mnyumba akhoza kuthandizidwa ndi akuluakulu ena omwe adziwa bwino zinthu pa nyumbapo. Ngati palibe mkulu wolamulira mnyumba, membala wamkulu aliyense pa nyumbapo amene adziwa bwino akhoza kusankhidwa kukhala oyankha.”

Kodi mkulu wolamulira mnyumba kapena banja ndani?

Dziwani kuti mkulu wolamulira mnyumba akhoza kapena sakhoza kukhala membala wa panyumbapo amene akutengako mbali mu bungwe lanu (ngakhale kuti mkulu wolamulira akhoza kukhala yemweyo).

Monga mwa tsamba 13 la *Buku Lomasulira*, "Mkulu wolamulira mnyumba kapena banja ndiye munthu amene nthawi zambiri mamembala apanyumbapo amuona kukhala wowalamulira. Wowalamulira ameneyo ndiye nthawi zambiri amapeza thandizo la chuma komanso wopanga ziganizo panyumbapo, koma muyenera kulola chiganizo cha mamembala apanyumbapo kuti wowalamulira iwo ndi ndani.

"Payenera kukhala m'modzi ndipo m'modzi chabe wolamulira panyumbapo. Ngati pali oposa pa m'modzi amene akuti ndiwolamulira, kapena ngati anthu ena pakati pa nyumbayo apereka mosemphanitsana amene akuti ndiye mkulu wolamulira mnyumbamo, pamenepo chionetseratu kuti mukufufuza pakati pa mabanja awiri kapena oposapo ndithu, koposa limodzi."

Malangizo a chionetsero chilichonse cha mukhadi lachiwerengero

1. Kodi banja lonse lapanyumba mukukhala mu tauni iti?
 - A. Chitipa, kapena Karonga
 - B. Neno, Nkhata Bay, Nsanje, Phalombe, kapena Rumphu
 - C. Chiradzulu, Machinga, kapena Thyolo
 - D. Balaka, kapena Mangochi
 - E. Chikwawa, kapena Dedza
 - F. Nkhotakota, kapena Salima
 - G. Mzimba, Ntcheu, kapena Ntchisi
 - H. Dowa, Kasungu, Mchinji, Mwanza, Zomba, kapena Zomba City
 - I. Blantyre, Lilongwe City, kapena Mulanje
 - J. Blantyre City, Lilongwe, kapena Mzuzu City

Pokhapo mukufuna kutero, musafunse funsoli molunjika kwa oyankha. Koma m'malo mwake, lembani yankho monga mwa nzeru ndi kuona kwa inu kuti nyumbayo ya wofunsidwa ili mu boma iti.

2. Kodi panyumba pano pali mamembala angati?
- A. Seveni kapena opitilirapo
 - B. Sikisi
 - C. Asanu
 - D. Anayi
 - E. Atatu
 - F. Awiri
 - G. M'modzi

Musafunse funsoli molunjika kwa oyankha. Koma m'malo mwake, lembani yankho monga nambala ya mamembala apanyumbapo imene mwalemba pa "Pepala Lakumbuyo Logwiritsa Ntchito".

Monga mwa tsamba 12–13 la *Buku Lomasulira*, "Nyumba akhoza kukhala munthu m'modzi ozikhalira yekha, kapena gulu la anthu, amene ndi abale kapena si abale, okhala pamodzi ngati anthu amodzi amene pakati pa iwo pali mgwirizano wokhala pamodzi panyumbapo (ndiko kuti, agawana kapena agwirizana pa chiyesero chimodzi ndalama).

"Tanthauzo lodziwika bwino la *panyumba* kapena *banja* ndilo 'gulu la anthu okhala pamodzi, naika ndalama zao, ndipo amadya onse pamodzi kosachepekera kamodzi pa tsiku lililonse'.

"Ndikothekera kuti anthu amene ndiwosakhala mamembala apanyumba kapena banja lofunsidwa akhoza kumakhala ndi banja lofunsidwalo panthawi ya kufunsa kumeneku. Pa nthawi zambiri – koma osati nthawi zonse – wina wake amene sakhala panyumbapo kapena ndi banja lofunsidwalo pa nthawi ya kufunsa kumeneku si ali membala wa panyumbapo kapena banjalo. Onani munsimu matanthauzo *membala wa panyumba kapena banja*, ndiko kuti, amene ali ndi amene si ali wa panyumbapo kapena pa banjapo.

"Mamembala mnyumba kapena banja sikuti ayenera kukhala pachibale chifukwa anabadwa ku makolo amodzi kapena kuti ali pa chikwati ai. Mbali yina, sikuti onsewo amene ali abale ndipo akukhala pa laini pamodzi kapena kukhala pamodzi ndi mamembala apanyumba kapena banja limodzi. Abale awiri onse okwatira komanso okhala ndi ana amene akhala mnyumba imodzi akhoza kapena sakhoza kupanga mgwirizano wosungira nyumba pamodzi. Ngati iwo sakutero, iwo ayenera kutengedwa ngati manyumba kapena mabanja awiri."

"Pali kusiyana pakati pa *banja* ndi *apanyumba kapena apa banja*. *Banja* lionetsa ubale wokhalirana pamodzi, ubale wochokera ku kholo limodzi, ndi chikwati. *Panyumba kapena banja* panopa mauwa akugwiritsidwa ntchito

kutanthauza gulu la chuma. Pamene mabanja ndi apanyumba kapena banja ndi amodzi, sikuti nthawi zonse akhalabe amodzi ofanana. Inu wowerengetsera muyenera kukhala maso ndi kugwiritsa ntchito zopatsidwa zonena pa umembala wa panyumba kapena banja kuona ndi kuti mudziwe kuti ndi anthu oti amene ali apanyumbapo kapena banjalo.

“Ngati mwamuna ndi wamitala komanso mabanja okhala ndi achibale ena, mamembala apanyumba atha kukhala mnyumba ziwiri kapena zopitirirapo. Ngati nyumbazi ziri pa laini imodzi kapena pa malaini apafupi, ndiponso ngati iwo ali ndi mgwirizano wosungira pamodzi nyumba nakhalanso ndi chiyesero chimodzi cha ndalama, ndiko kuti onsewa onse ayenera kuyesedwa ngati a nyumba kapena banja limodzi.

“Powerengera mamembala a panyumba kapena banja, kumbukirani:

- “Ndikotheka kuti mkulu wolamulira mnyumba kapena banja sakhala pompo pa nthawi ya kufunsa kumeneku. Iye mwina akhoza kumakhala ndi kugwira ntchito, ya kanthawi kapena yokhalitsa, m’dera lina la Malawi kapena ku dziko lina
- Ana a sukulu zogona komweko koma amene amakhala panyumba zofunsidwazo ayenera kuwerengedwa ngati mamembala apanyumba kapena banja lofunzidwa limenelo
- Musawerengereko asilikari, akaidi, kapena anthu ena amene akukhala kumalo kwina (monga zigawo zokhazikitsidwa pazokha) ndi onse wosakhala kuti umoyo wao ukudalira panyumba kapena banja pomwe mukufunsapo
- Ena mwa mamembala okhala panyumbapo kapena pa banjapo mwina si abale awo a mkulu wolamulira mnyumba kapena banja. Mwa chitsanzo, wantchito wokhala pompo pa nyumba kapena banja lomwe mukufunsa ndi membala wa panyumba kapena banja mukufunsa ngati iye alibe nyumba yakeyake kwina kulikonse kumene iyeyo ndiye mkulu wolamulira kapena kumene iye adalirako
- Antchito, kapena aganyu, ndi iwo wolipira kukhala pompo (anthu omwe amalipira kukhala panyumba pa wofunsidwayo) iwowa sayenera kuwerengedwa ngati mamembala mnyumba kapena banja lofunsidwa ngati iwo ali ndi mnyumba kapena banja lao kwina kwake kumene iwo ndiwo akulu wolamulira kapena kumene iwo adalirako
- Ana okhala ndi achibale ena (mwa chitsanzo, azakhali, kapena amalume kapena abambo akulu/abambo aang’ono) sayenera kuwerengedwa ngati mamembala apanyumba kapena banja lofunsidwa. Koma iwo ayenera kuwerengedwa ngati mamembala apanyumba kapena banja la azakhali/amalume kapena abambo akulu/abambo aang’ono”

Monga mwa tsamba 4 la 2016/17 IHS Household Questionnaire, “Pangani mndandanda wa anthu onse amene nthawi zambiri amakhala pamodzi ndipo amadya zakudya zao pamodzi mnyumba kapena banja ili, kuyambira ndi mkulu wolamulira mnyumba kapena banja [ndi (mkulu pa onse) wa amwao].

“Pofuna kupanga mndandanda wabwino wa anthu onse olumikizana ndi mnyumbamo kapena banjalo, gwiritsani ntchito mafunso awa:

- “Choyamba, ndipatseni maina onse a mamembala apabanja lanu lapafupi amene nthawi zambiri amakhala ndi kudya zakudya zao pano
- Tsopano, ndipatseni maina a wina aliyense amene ndi m’bale wanu kapena mamembala ena amnyumbamu kapena banja amene nthawi zambiri amakhala ndi kudya zakudya zao pano
- Kodi pali anthu ena amene si ali pano tsopano koma iwo nthawi zambiri amakhala ndi kudya zakudya zao pano? Mwa chitsanzo, mamembala apanyumbapo kapena banja omwe akuchita maphunziro kwina kapena anapita kwina
- Tsopano, ndipatseni maina a iwo onse osakhala abale anu kapena ena a mamembala apanyumba kapena banja, koma amene nthawi zambiri amakhala ndi kudya zakudya zao pamodzi pano, monga antchito, anthu wolipira ndalama kukhala nanu mnyumba yanu, kapena ena osakhala abale anu
- Musalembe antchito omwe ali ndi nyumba kapena banja kwina kwake, kapena alendo ocheza nao kwa kanthawi kochepa chabe ndipo iwo ali ndi nyumba kapena banja kwina kwake”

3. Kodi yanthawi ya nyengo yakutentha ikafika monga mu Oktoba, mukulu wolamulira pa nyumba amagona poti?
- A. Nsalu ya chitenje, saka ya thumba la fataleza kapena la mbeu, zovala, palibe, kapena zina
 - B. Gombeza chabe
 - C. Gombeza ndi nsalu zapabedi, kapena nsalu zapabedi chabe

Buku Lomasulira silipereka mfundo zina zapadera zokhudzana ndi funso ili.

Monga mwa tsamba 13 la *Buku Lomasulira*, "Mkulu wolamulira mnyumba kapena banja ndiye munthu amene nthawi zambiri mamembala apanyumbapo amuona kukhala wowalamulira. Wowalamulira ameneyo ndiye nthawi zambiri amapeza thandizo la chuma komanso wopanga ziganizo panyumbapo, koma muyenera kulola chiganizo cha mamembala apanyumbapo kuti wowalamulira iwo ndi ndani.

"Payenera kukhala m'modzi ndipo m'modzi chabe wolamulira panyumbapo. Ngati pali oposa pa m'modzi amene akuti ndi wolamulira, kapena ngati anthu ena pakati pa nyumbayo apereka mosemphanitsana amene akuti ndiye mkulu wolamulira mnyumbamo, pamenepo chionetseratu kuti mukufufuza pakati pa mabanja awiri kapena oposapo ndithu, koposa limodzi."

Dziwani kuti mkulu wolamulira mnyumba akhoza kapena sakhoza kukhala membala wa panyumbapo amene akutengako mbali mu bungwe lanu (ngakhale kuti mkulu wolamulira akhoza kukhala yemweyo).

Kumbukirani kuti mukudziwa kale dzina la mkulu wolamulira mnyumba kuchokera pa zomwe zalembedwa kale pa "Pepala Lakumbuyo Logwiritsa Ntchito". Motero, musafunse kuti, "Kodi munthawi ya nyengo yakutentha ikafika monga mu Oktoba, mukulu wolamulira pa nyumba amagona poti?". M'malo mwake, gwiritsani ntchito dzina lake loyamba kapena dzina lopeka la wolamulira, mwa chitsanzo: "Kodi munthawi ya nyengo yakutentha (monga mu Oktoba) Vincent amagona poti?"

4. Mu miyezi khumi ndi iwiri yapitayi, kodi mwamuna wolamulira pa nyumba (kapena mwamuna wa mkazi wolamulira) anagwirako zintchito za kanthawi, kapena ganyu, ngakhale kwa ola limodzi chabe?
- A. Inde
 - B. Palibe mwamuna wolamulira (ndipo mkazi wolamulira panyumbapo alibe mwamuna)
 - C. Ai

Monga mwa tsamba 54 la *Buku Lomasulira*, “*Ganyu* ndi ntchito yogwira kwa kanthawi kochepa mwina mwa masiku angapo kapena kwa kanthawi kena kalikonse. Kawirikawiri imakhala ntchito yosakulira ku minda kapena kulima galauza ya anthu ena ku minda zao. Ngakhale zili tero, ntchito ya ganyu ikhoza kukhala ntchito ina iliyonse ya kanthawi kochepa monga, kumanga ndi kulima mu dimba.

Monga mwa tsamba 54 la *Buku Lomasulira*, ntchito ya ganyu sindiye kugwira ntchito kopanda dipo (chipeleganyu), ndiye kuti, “kugwirira ntchito mnansi/ mbale kopanda malipiro (ngati, mwa chitsanzo, ngati akudwala).”

Kumbukirani kuti mukudziwa kale dzina la mwamuna wolamulira (kapena mwamuna wa mkazi wolamulira) kuchokera pa zomwe zalembedwa kale pa “Pepala Lakumbuyo Logwiritsa Ntchito”. Motero inu musafunse kuti, “Mu miyezi khumi ndi iwiri yapitayi, kodi mwamuna wolamulira pa nyumba (kapena mwamuna wa mkazi wolamulira) anagwirako zintchito za kanthawi, kapena ganyu, ngakhale kwa ola limodzi chabe?”. M’malo mwake, gwiritsani ntchito dzina lake loyamba kapena dzina lopeka la mkulu wolamulira wa mwamuna (kapena mwamuna wa mkazi wolamulira), mwachitsanzo: “Mu miyezi khumi ndi iwiri yapitayi, kodi Vincent anagwirako zintchito za kanthawi, kapena ganyu, ngakhale kwa ola limodzi chabe?”

Pa zifukwa zomasulira mu khadi lachiwerengero, *mwamuna wolamulira (kapena mwamuna wa mkazi wolamulira)* ndiye kuti:

- Mkulu wolamulira panyumba kapena pa banja, ngati wolamulira ndi wa mwamuna
- Mwamuna/wokondedwa wa mkulu wolamulira panyumba kapena pa banja, ngati wolamulira ndi wa mkazi
- Palibe, ngati wolamulira ndi wa mkazi ndipo ngati alibe wa mwamuna/wokondedwa amene ali membala wa panyumbapo kapena pa banjapo

Monga mwa tsamba 13 la *Buku Lomasulira*, “Mkulu wolamulira mnyumba kapena banja ndiye munthu amene nthawi zambiri mamembala apanyumbapo amuona kukhala wowalamulira. Wowalamulira ameneyo ndiye nthawi zambiri amapeza thandizo la chuma komanso wopanga ziganizo panyumbapo, koma muyenera kulola chiganizo cha mamembala apanyumbapo kuti wowalamulira iwo ndi ndani.

“Payenera kukhala m’modzi ndipo m’modzi chabe wolamulira panyumbapo. Ngati pali oposa pa m’modzi amene akuti ndiwolamulira, kapena ngati anthu ena pakati pa nyumbayo apereka mosemphanitsana amene akuti ndiye mkulu wolamulira mnyumbamo, pamenepo chionetseratu kuti mukufufuza pakati pa mabanja awiri kapena oposapo ndithu, koposa limodzi.”

Dziwani kuti mkulu wolamulira mnyumba akhoza kapena sakhoza kukhala membala wa panyumbapo amene akutengako mbali mu bungwe lanu (ngakhale kuti mkulu wolamulira akhoza kukhala yemweyo).

5. Kodi mkazi wamkulu wolamulira (kapena mkazi wamkulu wa mwamuna wolamulira) akwaniritsa kuwerenga ndi kulemba Chichewa kapena Chingerezi?
- Ai
 - Chichewa chabe
 - Palibe mkazi wolamulira (ndipo bambo wolamulira panyumbapo alibe mkazi)
 - Chingerezi chabe, kapena zonse Chingerezi ndi Chichewa

Buku Lomasulira silipereka mfundo zina zokhudzana ndi funso ili. Makamaka, silionetsa kuti iye wowerengetsera ayenera kufunsa za chisonyezo ngati zinthudi ziliterodi kapena chitsimikizo pa za mkazi ngati wolamulira (kapena mkazi wa mkulu wa mwamuna wolamulira) kuti adziwadi kuwerenge kapena kulemba. Ichi chionetsa kuti muyenera kutenga mawu a oyankhayo, pokhapo, monga zakambika kale kumbuyoku, ngati pali china choonetsa kwa inu kuti yankho imeneyo siili yolondola.

Funso ili ikhudzana ndi kudziwa kulemba ndi kuwerenga, osati chabe kulemba kapena kuwerenga kokha.

Kumbukirani kuti mukudziwa kale dzina la mkazi wolamulira (kapena mkazi wa mkulu wa mwamuna wolamulira) kuchokera pa zomwe zalembedwa kale pa “Pepala Lakumbuyo Logwiritsa Ntchito”. Motero, musafunse kuti, “Kodi mkazi wamkulu wolamulira (kapena mkazi wamkulu wa mwamuna wolamulira) akwaniritsa kuwerenga ndi kulemba Chichewa kapena Chingerezi?”. M’malo mwake, gwiritsani ntchito dzina lake loyamba kapena dzina lopeka la mkazi wolamulira (kapena mkazi wamkulu wa mwamuna wolamulira), mwa chitsanzo: “Kodi Tamanda adziwa kuwerenga ndi kulemba mu Chichewa kapena mu Chingerezi?”

Pa zifukwa zomasulira mu khadi lachiwerengero, mkazi wolamulira (kapena mkazi wa mkulu wa mwamuna wolamulira) ndiye kuti:

- Wolamulira panyumba, ngati wolamulira ndi wamkazi
- Mkazi wamkulu/wokondedwa wa wolamulira panyumba, ngati wolamulira ndi wamwamuna
- Palibe, ngati wolamulira ndi wa mwamuna ndipo ngati alibe wa mkazi/wokondedwa amene ali membala wa panyumbapo

Monga mwa tsamba 13 la *Buku Lomasulira*, "Mkulu wolamulira mnyumba kapena banja ndiye munthu amene nthawi zambiri mamembala apanyumbapo amuona kukhala wowalamulira. Wowalamulira ameneyo ndiye nthawi zambiri amapeza thandizo la chuma komanso wopanga ziganizo panyumbapo, koma muyenera kulola chiganizo cha mamembala apanyumbapo kuti wowalamulira iwo ndi ndani.

"Payenera kukhala m'modzi ndipo m'modzi chabe wolamulira panyumbapo. Ngati pali oposa pa m'modzi amene akuti ndiwolamulira, kapena ngati anthu ena pakati pa nyumbayo apereka mosemphanitsana amene akuti ndiye mkulu wolamulira mnyumbamo, pamenepo chionetseratu kuti mukufufuza pakati pa mabanja awiri kapena oposapo ndithu, koposa limodzi."

Dziwani kuti mkulu wolamulira mnyumba akhoza kapena sakhoza kukhala membala wa panyumbapo amene akutengako mbali mu bungwe lanu (ngakhale kuti mkulu wolamulira akhoza kukhala yemweyo).

6. Kodi nyumba yokhalamo ili ndi denga lopangidwa ndi chiani? (onani ndipo lembani)
- A. Udzu
 - B. Malata, matayilosu adothi, konkili, mapulasitiki, kapena zina

Pokhapo mukufuna kutero, musafunse funsoli molunjika kwa oyankha. Koma m'malo mwake, lembani yankho monga mwa nzeru ndi kuona kwa inu kuti nyumbayo ya wofunsidwa ili ndi denga lopangidwa ndi chiani. Ndiko kuti, yesani pa inu nokha kuona denga limenelo. Ngati yankho siili kuoneka bwino monga mwa kuona kwanu, pomwepo funsani oyankha.

Monga mwa tsamba 56 la *Buku Lomasulira, nyumba* "ikhoza kunenedwa kuti ndi chomanga (chokhalitsa, cha kanthawi, kapena ya kumudzi) mmene anthu amakhala ndi kugona. Ikhoza kukhala khumbi, nyumba, sitolo yokhala ndi zipinda zogonako kapena zipinda kumbuyo kwake kapena m'mbali mwake, gowero ya mabango/maphesi kapena udzu monga zomwe asodzi ansomba amagwiritsako ntchito, kapena chomanga china chilichonse mmene anthu amagona.

"Nyumba kapena malo okhalamo opangidwa mwa dwachedwache ndi zinthu zambiri zimapezeka kwambiri m'malo akumidzi, pomwe makhumbi adwachedwache amamangidwira mamembala osiyana-siyana apanyumbapo kapena banjalo."

Monga mwa tsamba 56 la *Buku Lomasulira*, "Konkiriti ikhoza kuwerengedwa ngati *denga* imene pamwambapo pamakhala pophapatala [pamene] chomangidwacho chili ndi pansu posatsiriza pamwamba pake."

7. Kodi muli ndi gome pa nyumbayi?

- A. Ai
- B. Inde

Buku Lomasulira silipereka mfundo zina zapadera zokhudzana ndi funso ili.

8. Kodi panyumbapo pali makama angati?
- A. Palibe
 - B. M'modzi
 - C. Awiri kapena opitilirapo

Buku Lomasulira silipereka mfundo zina zapadera zokhudzana ndi funso ili.

9. Kodi muli ndi mipeni za malupanga (zikwanje/mapanga) pa nyumba pano?
- A. Ai
 - B. Inde

Buku Lomasulira silipereka mfundo zina zapadera zokhudzana ndi funso ili.

10. Kodi panyumbapo pali maselefoni angati omwe akugwira ntchito pa nyumba?

- A. Palibe
- B. Imodzi
- C. Awiri kapena opitilirapo

Monga mwa tsamba 58 la *Buku Lomasulira*, inu wowerengetsera muyenera “kukhala cheru pakudziwa mwini wake wa maselefoni ya mamembala apanyumbapo koposa chabe ya mkulu wolamulira mnyumbamo. Fufuzani kuti msonkhanitse mfundo zonse zokhudzana ndi maselefoni omwe eni ake ndi mamembala apanyumbapo.”